Mgonjetsi Wamkulu Ndi Wamphamvu

Mmawa wabwino, kwa inu. Ndi "Isitara Yokondwerera" kwambiri kwa aliyense wa inu! Ili ndi limodzi la masiku opambana kwambiri, mu kukumbukira chiukitsiro cha Ambuye wathu. Ilo ndi limodzi la masiku opambana a mbiriyakale ya dziko lapansi lonse. Ndi chiukitsiro. Ndipo ndife okondwa kwambiri kukhala pano, mmawa uno, pa tsiku lopambana ili. Ndipo kuwona dzuwa likutuluka, ndipo maluwa akutuluka kuchokera mnthaka, chirichonse chikuyankhula za Isitara.

Ndipo tsopano tiyeni ife tiweramitse mitu yathu mu mphindi imodzi chabe.

2 Atate Mulungu, mu Kukhalapo Kwanu ife tikubwera. Ndipo ife tikuyembekeza kuti Inu mutipatsa ife, mmawa uno, mdalitso pang'ono wowonjezera wochokera Kumwamba, kukhudza kwina kwapang'ono kwa Isitara mmiyoyo yathu yomwe; kuti, pamene ife tidzichoka pano, ife tikakhoze kunena, monga aja amene ankabwera akuchokera ku Emmau, "Kodi mitima yathu siinatenthe mkati mwathu, chifukwa cha Kukhalapo Kwake?" Pakuti, ife tikupempha izi mu Dzina Lake, ndi kwa ulemelero Wake. Ameni.

3 Cha mu bukhu lotsiriza, mutu wa 28 wa Uthenga wa Mateyu Woyera, ndipo ndime ya 7, ine ndikufuna kuti ndiwerenge kwa phunziro, pamene ife tikulowa mu msonkhano uwu.

> *Ndipo pitani mwamsanga, ndipo mukawauze ophunzira ake kuti iye wauka kwa akufa; ndipo, taonani, iye akupita patsogolo panu ku Galileya; kumeneko* inu *mukamuwona iye: taonani, ine ndakuuzani inu.*

4 Pakhala pali kutuma kwakukulu kochuluka kukuperekedwa kwa munthu ndi anthu a mdziko lino. Koma sipanayambe pakhalapo kutuma kofunikira kunaperekedwapo konga uku, "Pitani mukawauze ophunzira Ake kuti Iye wauka kwa akufa." Kumeneko ndi kutuma kwakukulu. Ndipo izi zinachitika mwanjira iyi, chifukwa chakuti pamayenera kukhala kugonjetsa kwakukulu, poyamba.

5 Pakhala pali anthu mmasiku athu, ndi mmasiku amene anapita, ndi mu mbiriyakale ya dziko lino, mmabwalo ake aakulu, otambalala a nkhondo; pakhala pali agonjetsi ambiri aakulu, zinthu zazikulu zochuluka zimene zakhala zikuchitika kwa mtundu wa anthu.

6 Mwachitsanzo, ine ndikuganiza, pamene ine ndimabwera ndikutsika mmawa uno, ndinadzuka molawirira, ndipo sindinakhale ndi mwayi woti ndiwerenge mokwanira. Chifukwa, ine sindimadziwa basi kuti ndi gawo liti, usiku wathawu, limene ife tikanadzakhala nalo lero, pakati pa abusa ndi ine, mu misonkhano. Koma pamene ine ndimabwera kuno, ine ndinadzipeza ndikuganizira za chimene, mmawa uno, chingakhale chopambana chimene ine ndikuchidziwa kuti ndinene kwa anthu Ake, ponena za uthenga. Ine ndinaganizira za ichi, "Pitani mukawauze ophunzira Ake." Tsopano, *ophunzira* Ake ndi "omutsatira" Ake. *Wophunzira* ndi "iye amene akutsatira." Ndipo ine ndinaganizira za phunziro ili, la, *Mgonjetsi Wamkulu Ndi Wamphamvu*.

7 Ndipo poganizira za agonjetsi aakulu amene ife takhala tiri nawo mdziko lino, ndi zinthu zazikulu zimene iwo achita popititsa patsogolo ndi kupangitsa kufewa moyo wa munthu. Ine ndimaganizira za Napoleoni wamkulu, mmbuyo mmasiku ake, momwe iye sanali kwenikweni munthu Wachifaransa, koma iye anali ndi chinachake mmalingaliro mwake. Choyamba, iye—iye ananyoza France, iye sankamukonda iye. Iye ankachokera ku zilumba. Koma iye anali ndi ganizo mmalingaliro ake, kuti, tsiku lina iye akanadzagonjetsa. Ndipo chifukwa chimene iye anali nazo izi mmalingaliro ake, iye amayenera kukhala ndi chinachake choti agwirirepo ntchito.

8 Kwa munthu aliyense, iwe usanagwire ntchito, iwe umayenera kukhala ndi cholinga chinachake, njira ina imzake, chinachake chimene iwe ukugwirirapo ntchitoyo, choti ugwirirepo ntchito, chinachake choti ugwiritse ntchito.

9 Ndipo monga ife tonse timadziwira, potenga mbiriyakale ya Hitler . . . kapena, osati ya Hitler, koma ya—ya Napoleon, kuti iye amayendera mwezi, ndi kusintha kwa nyenyezi. Iye ankagwira ntchito mwanjira imeneyo, ndipo anali kuyembekezera; chifukwa chakuti nthawi ina iye anachita chomwecho, ndipo iye anapeza chigonjetso. Ndipo iye anadzabwera ku France, ndipo iye anadzakhala wankhondo wamkulu. Iye anapha anthu ambiri, chifukwa chakuti iwo amalephera kuti agwirizane naye iye. Ndipo iye anayeretsa dziko lake lonselo, kuti pasakhale chirichonse chotsutsana ndi iye. Iye mwamtheradi anangolisesa ilo, chifukwa iye ankafuna kuti ilo likhale mwanjira imeneyo. Ngati iye sakanalipanga ilo kukhala mwanjira imeneyo, pakanakhala pali chinachake chikutsutsana naye nthawi zonse, ndi dongosolo lake lalikulu limene iye anali nalo mmalingaliro ake. Moyo wake womwe ukanakhala uli pa chiwopsyezo, chotero iye ankayenera kuti awupangitse ufumu wake wonse mwangwiro monga iye akanatha kuwupangira iwo.

10 Ine ndikuganiza tsopano kuti inu mukunditsatira ine mu izi, za Mgonjetsi wamkulu yemwe ine ndikumuganizira. Chirichonse mu Ufumu Wake chikuyenera kukhala cha Iye. Izo zikuyenera

kukhala mtima, moyo, ndi thupi, kwa Iye. Musakhale kalikonse kotsutsana ndi Iye. Chirichonse chimene chikanamatsutsana ndi Iye, Iye amayenera kuti achichotsemo icho. Iye amayenera kuti chirichonse mwamtheradi chikhale cha Iyeyo. Ndipo pamene . . .

11 Napoleon, iye anatenga zida, mizinga, mifuti, mifuti yaitali, malupanga. Ndipo iye anapita patsogolo ndi lingaliro limodzi ili, kuti iye akagonjetsa dziko lapansi. Ndipo mowoneka iye anachita zimenezo, pa usinkhu wa zaka sate-firi. Pamene iye anali mnyamata, iye anali munthu woletsa zinthu. Ndipo kutchuka kwake kwakukulu kunamupanga iye kukhala wakumva zayekha; ndipo izo zinamfika mmitsempha yake, kufikira kuti iye anafa pa usinkhu wa zaka sate-firi, ali chidakhwa. Kutchuka kwake, sanapirire nako. Ndipo ine ndikuganizira za munthu, amene pa usinkhu uwu, pa usinkhu wa zaka sate-firi, anagonjetsa dziko ndipo nkumwalira ali chidakhwa, chifukwa cha kutchuka kwake, ndipo anataya cholinga chenichenicho chimene iye amachimenyera. Iye anali—iye anali wa mtundu, kapena, osati mtundu, ine ndikhoza kutero, koma iye anali chida cha mdierekezi. Ndipo anali akuyesetsa kuti aligwetsere dziko pansi, ndipo iye analephera, pa sate-firii.

12 Koma, oh, Wankhondo wamkulu uyu, wamphamvu amene ine ndikuyankhula za iye, pa usinkhu wa sate-firi, anagonjetsa chirichonse chimene chinali pa dziko lapansi ndi ku—ku gehena. Pa usinkhu wa sate-firi, Mgonjetsi wamkulu ndi wamphamvu!

13 Ine ndikuganizira za nkhondo zazikulu zimene zakhala zikumenyedwa ku bwalo. Ife tikudziwa, kuti timalizitse ndi Napoleon, kuti iye anafika pa mathelo ake ku Waterloo. Iwo unali mwayi wanga, osati kale kwambiri, kuti ndikawone zofanizira zimene zinapangidwa za mabwinja a agaleta ake, ndi za amuna apa kavalo ndi za anthu, momwe iwo anayalidwira ku bwalo la nkhondo. Ndipo agaleta ataunjikana pamodzi, magudumu atasweka, kunja uko ku mabwalo, kumene ziwonetsero zazikulu izi zimapangidwako.

14 Ndipo ndi zosiyana bwanji: kuzindikira kuti munthu ameneyo pa zaka sate-firii, ndi chamanyazi chimene chiri uko mu chikumbutso cha nkhondo yake yaikulu ndi chigonjetso chake; ndipo kenako nkupita ku Yerusalemu, ndi kukayang'ana pa manda apululu, ngati chikumbutso cha Mgonjetsi wamkulu ndi wamphamvu.

15 Mwanjiraina imzake, pamakhala chinachake pankhani ya kugonjetsa. Ngati tiri ndi chinachake chimene ife tikumenyana nacho, ngati tiri ndi nthenda mthupi mwathu, ndipo ife tikumenyana ndi imfa ndi moyo, chimakhala chigonjetso bwanji pamene ife tiwona kuti yagonjetsedwa. Ngati ife tikumenyana ndi chizolowezi china chachikulu, kapena chinachake chachikulu chimene chikumatifooketsa ife, pamene potsiriza

mbendera zazikuluzo zikawuluka ndipo kuti tagonjetsa izo; zimatipatsa ife kumverera kotani, mkati mwathu, pakuti zikatero ife tikhoza kukhala mgonjetsi.

16 Tsopano ine ndikuganiza za nkhondo yotsiriza, ndipo momwe zinakhalira kuti Hitler anatenga Warsaw. Ndipo achi German ankaganiza kuti icho chinali chimodzi cha zigonjetso zazikulu zimene zinakhalapo, chifukwa chakuti wankhondo wawo wamkulu, Adolf Hitler, mwakamodzi anamiza zonse mu Warsaw, anagwetsera pansi milatho, ndipo mlatho waukulu unadzagwa. Nyuzipepala zinayika zithunzi zazikulu za kugwa kwa mlatho. Achi German anaguba mu msewu, ndipo anawomba ng'oma ndipo analiza malikhweru, ndipo ndege masauzande zinamudutsa pamutu pake, pamene iye anapambana chigonjetso chake choyambirira chachikulu. Atakhala pamenepo ngati Alexander Wamkulu, kapena Napoleon, kuti wagonjetsa dziko, koma kodi iye anakathera kuti? Mwamanyazi. Ndithudi, iye anatero.

17 Ine ndikukhoza kukumbukira pamene iwo anamanga Burma Pass yaikulu. Pakuyenera kuti. . . akafuna kuti awoloke phiri. Ena a anyamatawo akhala pano mmawa uno, mwinamwake, amene anadutsa mpita wawukulu uwu. Inali ntchito bwanji imeneyo! Ndi ntchito yeniyeni bwanji inatengera, ndipo ndi ntchito yeniyeni yotani iwo anaichita! Ndipo ndi ndalama zochuluka bwanji zimene iwo anagwiritsa ntchito kuti amange Burma Pass imeneyo, mamillioni a madola! Anyamata amene anataya miyoyo yawo, pochita zimenezo! Koma potsiriza, ndipo patapita kanthawi, pamene mtunda wotsiriza wa msewuwo unali utatha, ndipo pamene mpitawo unali utamalizidwa, mmene kufuula kwa chigonjetso kunamvekera kuchokera kwa anthu! Iwo anakhala ndi mpita woti aziwolokerapo podutsa pa phiripo, kuti akagonjetse.

18 Ine ndikuganiza za mpita wina, umene tsiku lina unachotsa moyo wa Ambuye wathu wodala. Uwo sunangokhala msewu pa dziko lapansi, koma uwo unali msewu wawukulu wotchedwa "msewu wawukulu wachiyero," umene wosayera sadzawolokerapo, koma iwo okha amene ayikidwa chidindo. Iwo okha amene ali kumbali imene Iye ali, adzadutsa msewu wawukulu uwu.

19 Zigonjetso zazikulu zakhala zikupambanidwa. Ambiri a ife lero tikhoza kukumbukira bwino za Nkhondo Yoyamba ya dziko lonse. Ine ndikukumbukira pamene ine ndinali mnyamata wachichepere, ine ndinkakhoza kumva malikhweru akuimbidwa; ndipo ngakhale alimi, mminda, anaimitsa akavalo awo, ndipo ankakupiza zipewa zawo. Iwo amafuula. Iwo amakuwa. Chinachitika ndi chiyani? Nkhondo inali itatha. Chigonjetso chinali chitapambanidwa. Chuma chachikulu chimene ife tinakhala tikumenyenirana, potsiriza ife tinali titapambana chigonjetso.

20 Ine ndikuganiza za nkhondo yomaliza ya dziko lonse iyi. Ine ndinkakhala tsidya lina la msewu. Ndipo pamene malikhweru anayamba kuwombedwa, anthu anathamangira panja; azimayi atavala maapuloni awo, ankawavula iwo, ndi kumawakupizira iwo mmwamba. Zipolopolo zinali zikuwuluka kudutsa mmitengo. Malikhweru akulizidwa. Magalimoto akuthamanga mmisewu. Anthu anali akugwa pa maondo awo, ndipo akukweza mmwamba manja awo. Iwo anafuula. Iwo ankalira. Chifukwa chiyani? Chifukwa nkhondo inali itatha. Ndipo odalawo, anyamata okondedwa amene anali kutsidya kwa nyanja, posakhalitsa anali akuti akhala akubweranso kumudzi kwawo. Chinali chigonjetso bwanji! Inali nthawi bwanji, ndipo zinali zokondoweza kwa mtima uliwonse! Chinali chikondwerero bwanji! Usiku umenewo, aliyense anali mu chisangalalo chimenecho, iwe ukanakhoza kukalowa mmalo odyera ndi kukadya, ndi kutulukamo ndipo osalipira izo, izo zikanakhala zabwinobwino. Iwe ukanakhoza kugwiritsa ntchito galimoto ya munthu winayo, izo zikanakhala zabwinobwino. Iwe ukanakhoza kufunsa zimene iwe umafuna, ndipo iwe mwinamwake ukanakhoza kulandira izo. Chifukwa chiyani? Chigonjetso chinali chitapambanidwa. Anyamata anali akubwera kwawo. Izo zonse zinali zitatha.

21 Ndipo ine ndikuganiza, m'bale wanga, izo ndi zoipa kwambiri kuti kumverera kwa mtundu umenewo sikumakhalitsa nthawi zonse. Koma, kwa Mkhristu, mmawa uno, chigonjetso chapambanidwa. Maberu achisangalalo akulira. Nkhondo yatha, pakati pa Mulungu ndi munthu. Chigonjetso chapambanidwa.

22 Chigonjetso chirichonse chisanapambanidwe, pamayenera kukhala mitengo yayikulu yoti ilipiridwe. Oh, mitengo bwanji! Ndipo nthawizina iyo imakhala yodula kwambiri, ndipo iyo imapangitsa zipsyera zazikulu, kuzing'ambira pansi. Koma, kuti tikhale ndi phiri, ife timayenera kukhala ndi chigwa. Ife tisanakhale ndi kuwala kwa dzuwa, ife timayenera kulandira mvula. Ife tisanakhale ndi kuwala, ife timayenera kukhala ndi usiku. Ife tisanakhale ndi cholondola, iwo ankayenera kukhala ndi cholakwika, kapena apo inu sibwenzi mutadziwa kuti cholakwika chinali chiti.

23 Koma kuti agonjetse ndi kupambana nkhondo yaikulu imene inayamba yapambanidwapo, Wina anatuluka kuchokera ku Ulemelero, zaka zambiri zapitazo. Ndipo Iye sanadzitengere pa Iyemwini mawonekedwe a Mngelo. Iye sanabwere ngati munthu winawake wamkulu. Koma Iye anali woti atsimikizire kuti izo sizimatengera mfuti yaitali ndi zipolopolo, ndi mabomba a atomiki, kuti ukapambane nkhondo. Iye anadziveka Yekha mu kudzichepetsa, monga kamwana kakhanda, ndipo anabadwira modyera ng'ombe. Kunalibe ngakhale malo akubadwa Kwake,

pamene Iye anabwera. Ine ndikufuna kuti inu muwone kusiyana kwa zipangizo za nkhondo, zimene Iye anagwiritsa ntchito.

24 Tsopano, mtundu wonse wa Adamu unali uli mu msinga. Anali ali kumeneko, opanda chiyembekezo, opanda Mulungu, opanda mwayi, opanda chifundo, opanda chirichonse chimene chikanati chiwathandize iwo. Adani aakulu, a kumalo a pansi a otayika, anali atawatsekera iwo mu mdima. Panalibepo njira yoti angatulukireko. Kunalibeko aliyense woti awathandize. Palibe chirichonse chimene chikanachitidwa. Izo zinkawoneka ngati anali mapeto akutaika, kwathunthu.

25 Koma Ngwazi yathu, Amene anatsika pansi kuchokera mmakonde a Ulemelero, kudzitsitsira pansi!

26 Pakuti, kunalibeko munthu pa dziko lapansi amene akanakhoza kuigwira ntchitoyo. Iwo onse anali, monga mwakuyankhula kwa chidziko, mu bwato limodzi. Ife tinali, tonse, "obadwa mu tchimo, owumbidwa mu kusaeruzika, tinabwera mdziko tikuyankhula mabodza." Ndipo palibe aliyense wa ife amene akanamuthandiza mzake. Ife tinali titaima opanda chithandizo, ogonjetsedwa, panali chisokonekero kumbali iliyonse, tonse sitimayanjana. Ife sitimatha kusunga malamulo ndi zikhalidwe, timalephera kuti tipeze zofooka zake ndi zina zotero, ife sitimatha kuchita zimenezo. Ndipo izo zinkawoneka ngati mtundu wonse wa anthu unali woti wasiyidwa kuti utaike.

27 Ndipo kenako Iye anadzabwera, Iye anadzatsika pansi. Chifukwa, "Iye anali pachiyambi," Baibulo linati, "Iye anali Mawu." Iye anali Logos imene inatuluka kuchokera mwa Mulungu. Ndipo Logos, pachiyambi, inali Mawu. Ndipo Iye anadzakhala Mawu. Kenako pamene Iye anadzakwera mmwamba pa tsiku lija la ulemelero la Isitara, Iye sanangokhala Mawu okha, koma Iye anadzakhala Wansembe Wamkulu wa Mawu Ake Omwe. Oh, ndi chinthu cha ulemelero bwanji, M'bale Neville! Tangoganizani! Iye sali Mawu okha, koma Iye ndi Wansembe Wamkulu wa Mawu Ake Omwe. Ife tingazikaikire bwanji izo? Ife tingayende bwanji kupita kwa Iye ndipo osakhulupirira kuti ife tilandira chimene ife tikuchipemphacho? Pakuti, Iye ndi Mawu ndi Wopembedzera wa Mawu! Logos inadzasanduka Mawu, ndipo Mawu anasanduka thupi; ndipo thupi lomwelo limene linali Mawu, linalandiridwa mmwamba mu Ulemelero, ndipo tsopano ndiye Wansembe Wamkulu akupanga mapembedzero, pa Iyemwini, kwa Mawu Ake.

28 Zimachititsa ndi zimenezo! Chimenecho ndicho chipangizo chimene Mpingo uli nacho. Ndi chida bwanji! Sipanakhalepo china chonga Chimenecho. Iye anali Mawu. Ndipo pamene Iye ankabwera, Iye anabadwira modyera ng'ombe. Iye anabwera kuti adzagwiritse ntchito chida cha c-h-i-k-o-n-d-i, chikondi, kuti adzagonjetse dziko lapansi; osati ndi

zipolopolo za ankhondo, osati ndi mifuti ya makina ndi akasinja. Koma Iye anabwera mkachitidwe kosiyana. Iye anabwera mmawonekedwe a chikondi. Iye anali chikondi cha Mulungu.

29 Nthawi ina, ngati mnyamata wachichepere, ine ndinkakonda kumaganiza kuti Khristu amandikonda ine, ndipo Mulungu ankadana nane ine; chifukwa chakuti Khristu anandifera ine, koma Mulungu anali ndi chinachake chotsutsana ndi ine. Koma ine ndinadzapeza kuti Khristu ndi mtima kumene wa Mulungu. "Mulungu analikonda kwambiri dziko lapansi, mwakuti Iye anampereka Mwana wake wokondedwa Yekhayo, kuti aliyense amene angakhulupirire mwa Iye asataike, koma akhale nawo Moyo Wamuyaya."

30 Tsopano Iye anabwera, poyamba, kuti adzagonjetse. Ndipo chinthu chimene mdierekezi anali atachiika pa dziko lapansi chinali udani. Ndipo Iye anabwera kuti adzagonjetse udani. Pamene ife tipambana nkhondo zathu, ndi zina zotero, mu nkhondo za mdziko lapansi, izo nthawizonse zimatisiyira, mosalekeza, udani; chifukwa, nkhondo za mtundu umenewo zimakhala za mdani. Koma Khristu anabwera ndi chikondi, kuti adzagonjetse udani, kuti adzawakonde iwo amene anali osakondeka. Iye anabwera ndi chida chosiyana. Ndipo Iye anadzichepetsa Yekha, "anadzipanga kukhala wotsikirapo pang'ono kuposa Angelo," kuti adzazunzike ndi imfa, ndi kuti adzapereke chitsanzo. Ndipo pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, Iye ankayenda pakati pa anthu.

31 Iye anali kutsimikizira zida Zake zankhondo, pamene Iye ankachiritsa odwala. Pamene Iye anatenga mabisiketi aang'ono asanu ndi zidutswa ziwiri za nsomba, ndi kudyetsa anthu faivi sauzande, Iye anatsimikizira kuti Iye anali ndi mphamvu pa atomiki iliyonse imene inalipo. Sikuti Iye anangomeretsa nsomba, koma Iye anakulitsa nsomba zophikidwa. Sikuti Iye anangomeretsa tirigu mu mabisiketi amenewo, koma Iye anakulitsa tirigu wophikidwa mu mabisiketi amenewo. Izo zinawonetsera kuti Iye anali Mgonjetsi wamkulu ndi wamphamvu uja! Iye sanangotenga madzi kuchokera pa chitsime, koma Iye anapanga madziwo kukhala, vinyo, kuchokera pa chitsime. Iye anatsimikizira kuti anali ndi Mphamvu zogonjetsera. Ndipo Iye ankakonda, ndipo chida Chake chinali chikondi. Tsopano zindikirani.

32 Ndiye pamene Iye anadzachita zimenezo, pamene Iye anadzaima tsiku lina pambali pa manda a Lazaro, ndipo pamenepo panali munthu, wakufa, ndipo ataikidwa mmanda masiku anayi. Ngakhale iwo amene anali pamenepo, anati, "ngakhale pano iye akununkha." Mphuno zake zinali zitagwera mkati, mphutsi za mthupi zinali zitakwawira mwa iye. Ndipo Yesu anaima pamenepo, ngati Mgonjetsi wamphamvu, pamene Iye ananena kwa Marita ndi Maria, pamene Iye anaima pamenepo, "Kodi Ine sindinakuuzeni inu, 'Ngati inu

mutangokhulupirira, inu muwona ulemelero wa Mulungu'?" Iye anali atangomalizitsa kuyankhula (pamene iwo anati, "mchimwene wathu anafa," ndi zina zotero), Iye anati, "Ine ndine chiukitsiro ndi Moyo! Iye amene akhulupirira mwa Ine, angakhale iye anali wakufa, komabe iye adzakhala ndi moyo. Ndipo aliyense amene angakhale moyo nakhulupirira mwa Ine, sadzafa konse. Kodi Ine sindinakuuzeni inu kuti Mphamvu yamuyaya, yodala ija ikukhala mkati mwa Ine?" Iye sanangopanga maneno, Iye anali wothekera kuchita chirichonse chimene Iye amanena, pakuti Iye anali Mgonjetsi wamphamvu.

33 Amakhala mwa Iye, akuzibisa, ataphimbidwa ndi mnofu wa munthu, ngati munthu, koma mkati mmenemo simumakhala winanso koma Mulungu Wamphamvuzonse, Iye wamkulu ndi wamphamvuyo. Iye amakhoza kulenganso. Iye amatha kulenga zinthu zatsopano. Iye amatha kuyankhula, ndipo chinthu chimene Iye wachipempha chimatha kupatsidwa mphindi yomweyo. Koma, Iye anadzichepetsa Yekha, Iye anakhalabe wotsika. Iye ankafuna kuti apereke chitsanzo. Iye ankafuna kuti akhale mtundu woyenera wa Mgonjetsi, ndipo Iye anakhaladi. Tsopano, Iye anadzitsimikizira Yekha kuti anali.

34 Monga ine ndakhala ndikunenera kawirikawiri mu misonkhano yanga, mwinamwake izo zikhoza kuchitira umboni mmawa uno, mu gulu lino la anthu, pa mmawa uno wokongola wa Isitara. Dona, wa mpingo winawake umene sumakhulupirira mu kuvomereza Magazi a Ambuye Yesu. "Ngati Magazi sakhetsedwa, sipangakhalepo chikhululukiro cha tchimo." Iye anali kundiuza ine kuti Munthuyo anangokhala mneneri, Munthu wodabwitsa, ndipo ine ndimamupanga Iye kukhala Waumulungu. Ine ndinati, "Iye anali Waumulungu. Iye anali Mulungu."

Iye anati, "Inu mumayesera kumupanga Iye kukhala wamkulu kwambiri."

35 Ine ndinati, "Palibepo mawu amene angakhoze kufotokoza ukulu Wake!" Lirime la munthu silinayambe lapezapo kufotokoza kwake!

36 Ndikuyankhula ndi munthu tsiku lina, kazembe wochokera ku Washington, DC, ndipo iye anati, pa umboni wawung'ono pa—pa kadzutsa kumene ife tinali limodzi, iye anati, "M'bale Branham, ine ndakhala ndiri wa chiLutera moyo wanga wonse. Koma," iye anati, "tsiku lina ndiri pa chitsitsimutso cha kachitidwe kachikale," anati, "Ine ndinagwada pansi pa guwa, ndipo ndinkafuna kukhala ndi chondichitikira ndi Mulungu." Iye anati, "Ndipo pamene ine ndinali pamenepo pa maondo anga . . . " Tsopano, uyutu ndi kazembe wochokera ku Washington amene anagwirapo ntchito pansi pa Purezidenti Cooledge. Ndipo pamene iye "anayang'ana mmwamba," iye anati, "Ine ndinawona masomphenya a Yesu." Iye anati,

"Ine ndimatha kuyankhula zinenero naini zosiyanasiyana, mosajejema." Iye anati, "Koma ine sindinapeze liwu limodzi loti ndiyankhule, mwa zinenero naini zonsezo." Iye anati, "Chotero ine ndinangokwezera mmwamba dzanja langa, ndipo Iye anandipatsa ine china chatsopano, choti ndiyankhuliremo." Iye anati, "Ine ndangowona kumene Ulemelero wa nkhope Yake."

37 Dona uyu akunena kwa ine, iye anati, "M'bale Branham, Yesu sanali kalikonse koma munthu basi, anangokhala mneneri."

Ine ndinati, "'Iye anali Mulungu,' mlongo wanga."

38 Iye anati, "Inu mumamupanga Iye kukhala Waumulungu, koma Iye sanali." Chotero iye anati, "Ali panjira akupita kumusi, akupita kokaitana . . . atagona, kumanda a Lazaro, Baibulo limati, 'Iye analira.'"

39 Ndithudi, Iye anali mtima kumene wa Mulungu. Iye anavutika monga ife timavutikira. Iye anali mnofu chimodzimodzi monga nafenso tiri mnofu. Iye anali nazo, mthupi Mwake, zokhumba zomwezo ndi zinthu zimene ife timazichita. Komabe, kuti akakhale Nsembe yangwiro, Iye ankayenera kuti achite zimenezo. Iye anatero. Koma ine ndinati . . .

Iye anati, "Iye analira, akupita ku manda a Lazaro."

40 Ine ndinati, "Koma, oh, dona, uko nkulondola. Iye anali Munthu, pamene Iye ankalira. Koma pamene Iye anadzaima pamenepo, pambali pa manda amenewo, pamene panagona wakufa wacheteyo; pamene thupi lovunda linagona, litakutiridwa ndi thewera; pamene Iye anati, 'Chotsanipo mwalawo.' Iye anadzikokera thupi Lake pamodzi, ndipo anati, 'Lazaro, tuluka!' Ndipo munthu amene anali wakufa, masiku anayi, anaimirira pamapazi ake."

41 Icho chinali chiyani? Chivundi chinadziwa Mpangi wake. Solo inadziwa Mbuye wake. Ndipo Mgonjetsi wamkulu ndi wamphamvu uja anatsimikizira pamenepo kuti Iye anali ndi Mphamvu ya imfa, ndi ku gehena, ndi ku manda.

42 Ndithudi, izo zimakondoweza mitima yathu! Inu mukakamba za kumenya zivinikiro za mbale, ndi kumaliza nyanga? Dziko likuyenera kukhala mu chikondwerero mmawa uno, chonga chimene sichinayambe chakhalapo, kukuwa ndi kufuula kwa anthu Ake, chifukwa ili ndi tsiku la chikumbutso la pamene Iye anagonjetsa mdani wotsiriza, ndipo nkutimasula ife akapolo kukhala amfulu.

43 Inde, Iye anali Munthu. Uko nkulondola. Iye anatsimikizira kuti anali Munthu, ndipo Iye anatsimikizira kuti anali Mulungu.

44 Usiku wina, pamene nyanja yaikulu, yaukali, imene yaitana miyoyo masauzande . . . Mwinamwake ena a amayi inu pano, mmawa uno, anyamata anu anafera mnyanja yaukali kunja

uko, iwo mwinamwake anamira pansi pa mafunde mu mabwalo aakulu a nkhondo a dziko lino. Ena a okondedwa anu akugona kunja uko, mwinamwake pansi pa nyanja.

45 Koma usiku wina pamene Iye anali atagona mu bwato laling'ono, ndipo mafunde akumenya pamenepo pa nyanja, ngati chotsekera cha botolo. Iye anadzuka, ndipo anadzaika phazi Lake mmphepete mwa bwato. Iye anayang'ana mmwamba akuyang'ana Kumwamba, anati, "Bata." Ndipo kwa mafunde, Iye anati, "Khalani bata!" Ndipo nyanja yamphamvu ija inachita bata kufikira kuti munalibe ngakhale khwinya mwa iyo. Ndithudi, Iye anali!

46 Ndi zoona kuti Iye ankamva njala ngati Munthu. Pamene Iye anatsika kuchokera m'phiri ndipo Iye anali ndi njala, akuyang'ana mu mtengo kuti apeze chinachake choti adye, Iye anali Munthu. Koma pamene Iye anadzatenga mabisiketi asanu aja ndi nsomba pang'ono, ndi kudyetsa faivi sauzande, Iye anali woposa Munthu.

47 Pamene Iye anafa zaka naintini handiredi zapitazo, dzana, atapachikidwa pa mtanda, akufuula kufuna chifundo, "Mulungu Wanga, Mulungu Wanga, nchifukwa chiyani Inu mwandisiya Ine?" Iye anafa ngati Munthu. Koma zaka naintini handiredi ndi chakuti zapitazo, mmawa uno, Iye anatsimikizira chimene Iye anali! Iye anapereka chisindikizo chotsiriza cha Umesiya Wake pamene Iye anaphwasulira zingwe za imfa ndi hade pakati, ndipo nkuwuka kuchokera mmanda, mwachigonjetso, "Ine ndiri wamoyo kwanthawizonse! Ndipo, chifukwa ine ndiri moyo, inunso mudzakhala moyo!"

48 Ndi Ameneyo Mgonjetsi! Inu mukakamba za kuchotsa maapuloni ndi kumawakupiza iwo? Anthu amati ndife amisala chifukwa chakuti timafuula ndi kuthamangathamanga, ndipo ife timakuwa ndi kufuula mokweza. Iwo sanayambe amvererapo kunjenjemera kwa chigonjetso cha Kumwamba, kuti, "Nkhondo yatha!" Mgonjetsi wathu, wamkulu ndi wamphamvu wapambana chigonjetso chirichonse! Iye akuima yekha, mmawa uno, wosati nkupikisana naye!

49 Pamene Iye anadzabwera ku dziko lapansi, iwo anampatsa Iye dzina lotsikitsitsa limene iwo akanamupatsa Iye, ngati "wotengeka." Iwo anamutcha Iye *Belezebule,* "kalonga wa ziwanda." Uko nkulondola. Iye anapita ku mzinda wotsikitsitsa umene ulipo mdziko, Yeriko, ndipo munthu wochepetsetsa kwambiri mu mzindawo amachita kuyang'ana pansi kuti amuwone Iye. Koma pamene Mulungu, zaka naintini handiredi zapitazo, anamuukitsa Iye! Izo ndi zimene munthu anachita kwa Iye. Koma, ndi chida cha chikondi, Iye anamgonjetsa mdierekezi aliyense.

50 Ndipo Mulungu anamukwezera Iye mmwamba kwambiri, ndipo anampatsa Iye Dzina loposa dzina lirilonse limene

linatchulidwapo Mmiyamba ndi dziko lapansi. Dzina lirilonse Kumwamba limagwadira Dzina la "Yesu"! Mngelo aliyense, mfumu iliyonse, chirichonse chimagwadira ku Dzina la "Yesu"! Lirime lirilonse lidzamuvomereza Iye, bondo lirilonse lidzamugwadira Iye. Ndipo Iye anakwera mmwamba kwambiri, kufikira kuti Iye amachita kuyang'ana pansi kuti aziwona Miyamba. Ameneyo ndiye Mgonjetsi wamphamvu! Ameneyo ndi Iye amene anachita izo! Pamene Iye anachoka pa dziko lapansi, zitatha, tinali nazo usiku wathawu, Iye anali ndi mafungulo a imfa ndi hade akulendewera pa mbali Yake, ameni, "Musawope, Ine ndi Iye amene ndinali wakufa, ndipo ndiri wamoyo kenanso kwanthawizonse. Ndipo" (*ndipo* ndi mlumikizi) "Ine ndiri nawo mafungulo a imfa ndi hade, akulendewera *apa*." Kukamba za Mgonjetsi! "Ndipo, chifukwa Ine ndinagonjetsa, Ine ndinangokupangirani inu msewu wawukulu kuti muziyendamo."

51 Munthu anakanidwa kuchokera Kumwamba, misewu yayikulu inatsekedwa. Kunalibe misewu yayikulu. Koma, kumene kunalibe misewu yayikulu, Iye anabwera kuti adzapange umodzi. Oh, mai! Mzere woyamba unali wa ziwanda zokaikira, wotsatira unali wosankhana, wotsatira unali wodzikonda; dziko ili linakutiridwa ndi mizere ya mphamvu ya ziwanda; kenako matenda, nthenda. Koma pamene Iye anayamba kukwera kupita Kumwamba! Usiku watha ife tinali naye Iye akubwera kuchokera ku gehena, ali ndi mafungulo a imfa ndi hade pambali Pake. Mmawa uno ife tikumutengera Iye mmwamba. Aleluya! Pamene Iye anauka, Iye anali . . . Iye anapambana. Ndipo, pamene Iye ankakwera mmwamba, Iye anaphwanya mphamvu iliyonse ya mdierekezi imene imagwira pa munthu. Iye anakwera Mmwamba, ndipo anadzapereka mphatso kwa anthu, mphatso za Mzimu Woyera. Mgonjetsi wamphamvu! Iye akuima yekha, mmawa uno! Ndipo, pakati pa Iye ndi wokhulupirira aliyense, pali msewuwawukulu wodala wakale wachiyero umene olungama adzayendamo. Palibepo njira yothawirapo. Pali mzere umodzi wokha wodulidwa kuchokera ku Ulemelero. Iye anasiya Mphondero za Magazi pamene Iye ankayenda kudutsa mmakonde a mphamvu za ziwanda, ndipo anadzatipangira ife msewu wawukulu, kudutsa njira yonse. Iye akukhala Mmwamba, mmawa uno, ngati Mgonjetsi wamphamvu!

52 Anthu Ake akukhala ndi chikondwerero. Makumi a zikwi a iwo, kuzungulira dziko lapansi, akufuula chigonjetso.

53 Ine ndaziwonapo zakale izi zozizira zojowina matchalitchi ofunda akale. Ine ndikhoza kulingalira winawake akunena . . . Ine ndikuwonetsani mmene mungazitchotsere izo.

54 Kuno, mwamsanga pamene Nkhondo Yoyamba inatha, uthenga unali ukubwera mu msewu kuno, ukubwera pa basi ya

Greyhound. Iwo anati, "Phokoso lonseli ndi chiyani? Zonsezi ndi za chiyani?"

55 Ndipo mmodzi wa iwo anati, "Taonani kuno, nyuzipepalayo ndi iyi. Nkhondo yangotha kumene." Ndipo aliyense akulira ndi kumafuula.

56 Koma mkazi wina anati, "Oh, mai, nchifukwa chiyani iyo yatha chomwecho?" Anati, "Ngati iyo ikanangokhala utali wa masiku angapo," anati, "John ndi ine tikanapeza zinthu mophweka." Anati, "Ife tikanakhala titakhala pamenepo."

57 Panali mzibambo yemwe anali ataima kumbuyo kothera basi; anadzamugwira mkazi ameneyo, ndipo anatsala pang'ono kuti amutulutsire pa chitseko. Ndipo pamene a polisi anamumanga m'bamboyo, iye anati, "Chifukwa chimene ine ndinachitira zimenezo," iye anati, "mkazi ameneyu analibe aliyense kumeneko amene amamulabadira. Koma ine ndiri ndi anyamata awiri kumeneko." Iye anati, "Ine ndinalephera kuti ndizigwire ndekha."

58 Oh, m'bale! Ine ndiri ndi bambo anga kutsidya uko. Ine ndiri nawo okondedwa kutsidya uko. Ndi chinachake kwa ine, pamene Yesu anagonjetsa. Ine ndiri ndi mkazi. Ine ndiri ndi mwana. Ine ndiri ndi okondedwa anga. Mgonjetsi wamkulu, wamphamvu uja! Inu mukhoza kunditcha ine "woyera-wodzigudubuza" kapena "wachipembedzo wotengeka," chirichonse chimene inu mungafune. Koma, ine ndikaganiza kuti nkhondo yaikulu ija inatha, mtengo unalipiridwa, chigonjetso chinapambanidwa. Yesu anauka kwa akufa, chisindikizo Chake chomalizira cha umesiya Wake, chakuti izo zonse zatha. Iye ali wamoyo, mmawa uno, ali ndi mafungulo a imfa ndi hade. Ine ndiri ndi okondedwa amene ali kutsidya kuwoloka malire kutali uko. Ine ndiri pa msewu wawukulu wakale wapamwamba uwu, ndikuyenda chokwera kupita kuti ndikawawone iwo. Musaganize kuti ine ndachita misala. Oh, koma ndine wokondwa kwambiri kuti zonse zatha! Iyo ndi ntchito yomalizidwa.

> Pokhala moyo, Iye anandikonda ine; pakufa,
> Iye anandipulumutsa ine;
> Ataikidwa mmanda, Iye anandinyamulira
> machimo anga kutali;
> Powuka, Iye anandilungamitsa mwaulere
> kwanthawizonse;
> Tsiku lina Iye akubwera, O tsiku la ulemelero!

59 Ubatizo wodala uwu wakale wa Mzimu Woyera, ndi wakuti utitsogolere ife pamene tikukwera mmwamba mu msewu wawukulu wakale wopambana uwu, oh, Izo ndi za ulemelero bwanji! Ine ndingachite nazo bwanji manyazi Izo? Ine ndikuima ndi Paulo Woyera, mmawa uno, ndikunena ichi, "Ine sindikuchita manyazi ndi Uthenga wa Yesu Khristu, pakuti Iwo ndi Mphamvu ya Mulungu ku chipulumutso." Iwo ndi Mphamvu

pa matenda. Iwo ndi Mphamvu pa imfa. Iwo ndi Mphamvu pa manda.

60 Pamene mtumwi wokhwimitsa uja, wakale anafika pa mapeto a msewu wake, ndipo iwo nakumba manda ake kunja uko, ndipo imfa inali ikumuyang'ana iye mmaso, iye anaseka pamaso pomwe pa iyo. Iye anati, "Imfa, mbola yako ili kuti? Manda, chigonjetso chako chiri kuti?" Kenako iye anafuula matamando a Mulungu, "Koma mathokozo akhale kwa Mulungu Yemwe amatipatsa ife chigonjetso kudzera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu!"

61 Mgonjetsi wamphamvu kwambiri amene anayamba wakhalapo moyo, Mgonjetsi wamphamvu amene anayamba wafapo, pakuti Iye anali Mmodzi yekhayo amene akanagonjetsa; kufa, ndi kudzagonjetsa imfa iyo kumene, ndipo nawukanso mwachigonjetso! Iye anatsimikizira chimene Iye anali. Icho chinali chisindikizo chotsiriza cha umesiya Wake.

62 Ndipo tsopano, mwamwayi, ngati pangakhale winawake mchipinda chino mmawa uno, amene ali membala wofunda wa mpingo, ndipo sakudziwa chimwemwe chakuti nkhondo inatha. Anthu amafuula, anthu amasangalala, anthu amalira! Inu mukuti, "Vuto lawo ndi chiyani iwowo?" Iwo amadziwa kuti chinthucho chatha. Izo zonse zatha! Ndithudi! Ife tiri [M'bale Branham akuwomba mmanja—Mkonzi] kuwomba ng'oma. Ife tikufuula malipenga, ndipo Uthenga ukupita. Ulemelero ndi Mphamvu ya Mulungu zadziwika. Ndipo iyo ndi ntchito yotsirizika, mgwirizano wasainidwa; ulemelero kwa Mulungu, Khritsu anasainira iwo ndi Magazi Ake Omwe! Nkhondo yatha. Chigonjetso chapambanidwa. Ine sindinapambane icho; Iye anapambana icho. Ine ndangokhala wokondwa nazo izo. Mai!

63 Pamene ena a anyamata amenewo ankabwera kuchokera ku tsidya la nyanja, iwo amandiuza ine, pamene ngalawa inkabwera mu New York, basi pamene iyo inkafika pa doko, iwo anayang'ana chokweza pamenepo ndipo iwo anawona Chosemedwa cha Ufulu. Icho ndi chinthu choyambirira chimene iwe umachiwona, chikudzuka mmwamba. Iwo anadzuka, ena a iwo ankhondo akale olumala anatulukira panja pamwamba pa ngalawayo, kuti iwo athe kuchiwona icho. Ndipo pamene iwo anayamba kuwona Chosemedwa cha Ufulu icho, iwo anayamba kulira. Iwo analira. Iwo sakanachitira mwina. Munthu wamkulu wonenepa anaima pamenepo, munthu wamkulu wa dzanja lokhakhala, akunjenjemera ndi kumadzigwedeza. Iwo sakanatha kudziletsa kutengeka kwawo. Chifukwa chiyani? Iyo inali mbendera ya ufulu. Kuseri kwa Chosemedwa cha Ufulu chimenecho, kunali . . . kunali bambo, amayi, okondedwa, wokomamtima, mkazi, mwana, onse a pa dziko lapansi lino amene ankatanthauza zokoma kwa iwo, anangokhala kuseri kwa icho. Ndipo basi iwo asanalowe, iwo anazindikira, kuti linali dziko la amfulu ndi kwawo kwa olimbamtima.

Ndithudi, izo zingagwedeze kutengeka kwanu, mbendera yakale ija ikukupiza. Taganizani za zimenezo, wankhondo wakale wa zipsyera akubwera pa doko! Ndithudi, iyo inali nthawi yopambana.

64 Koma, oh, m'bale, amodzi a mmawa awa, pamene Ngalawa yakale ya Zioni idzawomba, ndipo ine nkudzawona mbendera iyo itaima pamenepo, Mtanda wakale wotunduzidwa! Pamene mphepo zidzakhala zikukupiza mbendera zake zotuwa zakale, pamene iyo idzakhala ikuyenda kudutsa chifunga cha imfa. Chidzakhala chigonjetso bwanji chimenecho! Bwanji, nzosadabwitsa ife sitingathe kudzigwira kutengeka kwathu apobe! Chinachake chachitika; ife tasanduka mzika zimzawo. Chinthucho chamalizika.

65 Pamene iwo anamanga mlatho waukulu wa pakati pa Kumpoto ndi—ndi—ndi—ndi Kummwera kwa Australia, wochokera ku Sidney, kupita Kummwera kwa Sidney. Momwe munthu aliyense anatengera . . . Bwanji, iwo anapita pa dziko lonse, kuyesetsa kuti akamupeze munthu woti achite izo. Ntchito imeneyo inali yayikulu kwambiri, chifukwa iwo ankati panalibe munthu akanaichita iyo. Potsiriza, munthu wochokera ku England anati, "Ine ndiigwira ntchitoyo." Ndipo pamene iye anafika kumeneko kuti akaigwire ntchitoyo, iye anayesa boti lirilonse limene limakalowa pa mlathowo. Kutchuka kwake kunali pangozi. Iye anayeza matope onse ndi chirichonse chimene chimakalowa pansi. Iye anapita uku ndi uku, ndipo anakapeza zopambana zimene iye akanazipeza; iye anapeza amakaniko apamwamba kwambiri, azasayansi apamwamba kwambiri, apamwamba kwambiri aliwonse amene iye akanawapeza, pomuzungulira iye. Ndipo, potsiriza, pamene mlathowo unadzatha, ndipo tsiku nkufika limene iwo umayenera kuti uyesedwe.

66 Otsutsa anaima patali kumbali imodzi, ndipo iwo anati, "Iwo sulimba. Iwo ugwera pansi. Pansipo pali mchenga wambiri."

67 Koma iye anakumba pansi, pansi, pansi, pansi kwambiri. Iye anali ndi chidaliro. Iye amadziwa kuti chirichonse chinali chitayezedwa. Ndipo iye anati, "Ine ndiyamba kuwoloka kaye, ndekha." Ndipo pamene iye amayenda kuwoloka mlathowo, pamaso pa ameya, ali kumbuyo monga choncho; ndipo sitima zazikulu, pafupifupi sikisi zitandondozana, zikubwera modutsa, zikugwedeza mlathowo. Bambo wamkulu amene anamanga iwo, amayenda kutsogolo kwa zochitika izi, monga chonchi, "Ngati iwo uti ugwe, ine ndiri nawo iwo." Koma iye anali nacho chidaliro.

68 Umo ndi momwe Ambuye wathu wodala anachitira pamene Iye ankapanga Mpingo Wake! Iye anayesa boti iliyonse, chirichonse chimene chimakalowa mwa Iwo, pakuti Iwo umayenera kukhala wotsukidwa ndi Magazi! Ndipo

mmodzi wa wotsutsa anali ataima pambali, anati, "Gulu ilo la oyera odzigudubuza, iwo sazikwanitsa izo." Koma limodzi la masiku aulemelero awa! Mgonjetsi wamkulu, wamphamvu uyu akuyenda kutsogolo kwathu lero, mwachipambano! Akamusiya iye kuti anjenjemere, apange zimene iye akufuna, Iye. . . Apo sipadzakhala kuterereka kulikonse mwa iye, kulikonseko, pakuti Iye wakonza njira, ndipo anaimalizitsa iyo. Ndithudi!

69 Ife timalingalira lero pa zonena za anthu, timatengera malingaliro athu pa zinthu za mdziko. Koma ndiloleni ine ndikuuzeni inu chinachake, m'bale, musalole ine ndidzachite manyazi ndi Uthenga! Oh, m'bale, ine ndangokhala wachikale, wobadwa mwatsopano, wobadwa mwa Mzimu Woyera, wa Mzimu wa Mulungu. Ine ndinabadwa mwanjira imeneyo, ndizo zonse zimene ine ndiri, ndi zonse zimene ine ndikufuna kuti ndidzakhale.

70 Nthawi ina, osati kale kwambiri, panali mtsikana amene anapita ku koleji. Ndipo iye anali mtsikana wokoma, wamng'ono. Ndipo pamene iye anabwerera kunyumba, iye anabwera ndi ena a malingaliro ake akukoleji limodzi naye.

71 Ndipo mwinamwake, mmawa uno, ena a inu munabwera ndi malingaliro anu akunja limodzi nanu. Mwinamwake mwabwera, ku tchalitchi ndi, malingaliro anu ochulukawo. Chabwino, achotseni iwo, ndicho chinthu chopambana chimene ine ndimadziwa kuchichita.

72 Kenako mtsikana uyu, pamene sitima inadzaima patsogolo. Iye anabwera ndi mtsikana wamng'ono limodzi naye, wina wa mtundu wa mashasha aang'ono awo, inu mukudziwa, monga mtundu wa Elvis Presley. Ndipo pamene iye anali ataima pamenepo, inu mukudziwa, pa sitimapo, mayi ake anali, ali panja; mayi wokalamba ataima pamenepo, ali ndi zipysera paliponse, pa nkhope yake; wamng'ono, wa mapewa akugwa; atavala ka diresi ka biriwita kakang'ono, kashawelo kakang'ono kali pa mapewa ake. Ndipo shasha wamng'ono uyu amene anali ndi iye, mtsikana wina uyu, anayang'ana pansi, ndipo anati, "Chabwino, ndi ndani wowoneka momvetsa chisoni uyo, nkhalamba yonyasa yosawukayo?"

73 Chabwino, inu mukudziwa, zimenezo zinamuchititsa manyazi kwambiri mtsikanayo, iye anati, "Ine sindikudziwa," chifukwa iye anangokhala wosasamala kwambiri, ndipo anali ndi malingaliro ambiri a chidziko mmutu mwake. Ndipo awo anali amayi ake omwe.

74 Pamene iye anatsika sitimayo, amayi aang'ono okalambawo anathamanga, kuti akamukumbatire iye. Iye anati, "Oh, wokondedwa, Mulungu adalitse mtima wako waung'ono." Ndipo iye anatembenuza nsana wake ndipo nayamba kumachokapo, ngati kuti iye samawadziwa iwo. Iye amachita manyazi, chifukwa amayi ake anali onyasa kwambiri.

75 Ndipo zinachitika kuti, kondakitala wa msitima imeneyo, amaidziwa nkhaniyo. Iye anayenda kupita pamenepo, ndipo anadzaika manja ake pa mapewa a mtsikanayo, anamutembenuzira iye kwa anthu amenewo, anati, "Manyazi pa iwe! Manyazi pa iwe!" Anati, "Ine ndinalipo pa nthawi imene amayi ako anali okongola ka teni kuposa momwe iwe wakongolera." Anati, "Iye anali . . . ine ndinkakhala moyandikana nanu." Ndipo anati, "Iwe unali khanda, ndipo iwe unali uli mmwamba mnyumba mu bedi yako. Ndipo amayi ako anali akuyanika zovala kuseri kwa nyumba." Ndipo anati, "Mwadzidzidzi, chumuni chinayaka moto, ndipo nyumba yonseyo inali itakolera moto. Ndipo pamene amayi ako achichepere anadzathamangirako, ndipo nadziwa kuti iwe unali mmwambamo, mmwamba uko." Anati, "Iwo anafuula, ndipo anayesetsa kuti amugwire iye. Koma iye anataya zimene anali nazo, kuzichotsapo, ndipo anathamanga kudutsa mmalawi amoto amenewo, kukwera kupita mmwamba; ndipo anavula zovala zake pa thupi lake, ndipo anakukutira iwe ndi zimenezo. Ndipo apa iye anali akubwera, akubwerera kudutsa mmalawi amotowo, atakunyamula iwe. Ndipo iye anakakomokera, panja, ali ndi iwe mmanja ake." Ndipo anati, "Iye anatenga chimene chikanamutetezera iye, ndipo anakutetezera nacho iwe." Ndipo anati, "Chifukwa chimene iwe uli wokongola lero, ndi chifukwa chimene iye aliri wonyasa. Ndipo, iwe ukufuna kuti undiuze ine, iwe ungachite manyazi ndi zipysera zimenezo pa amayi ako?"

Ine ndikuganiza lero:

> Ngati Yesu anganyamule mtanda yekha,
> Ndipo dziko lonse lizipita mwaufulu?
> Pali mtanda wa aliyense,
> Ndipo pali mtanda wa ine.

76 Ngati Yesu ankatengedwa kuti anali "Belezebule," ndi dziko lino, Iye anasekedwa ndi kunyozedwa, ndipo anapachikidwa pa mtanda, anachititsidwa manyazi chifukwa cha ine, ine ndiri wokondwa mowonjeza kusenza chitonzo cha chiyero Chake. Inde, bwana. Mukhoza kunditcha, "Woyera wodzigudubuza!" chirichonse chimene inu mungafune kunditchula, ndemanga iliyonse imene mungafune kuyipanga. Izo sizingaimitse izo mpang'ono pomwe. Ine ndangokhala wokondwa, mmawa uno, kuti, mu mtima mwanga, Khristu woukitsidwa akukhala moyo ndipo akulamuliramo. Ine ndi mmodzi wa mzika Zake. Ine ndikudalira kuti inunso muli.

77 Nthawi yathu yatha tsopano. Pano ndi ndendende seveni koloko, pamene ife tinati tidzakhala tikubalalika. Misonkhano yopitiriza ikhala ikuyamba mu pafupi maora awiri, tsopano, pa hafu pasiti naini.

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu, kamphindi chabe, mu pemphero.

78 Atate Akumwamba Odala, maminiti forte-faivi adutsapo, Mawu aperekedwa. Mitima yathu ndi yokondwa. Chikondwerero chiri mkati; osati kungokhala chikondwerero cha tsiku limodzi, koma chikondwerero Chamuyaya! Mu Ulemelero, Angelo akuyimba. O Mulungu, Mpingo, mwachipambano, ukuyimba. Mabelu a chimwemwe akulira. Miyoyo imene nthawiina inaweruzidwira ku imfa, ndipo kuti ikafe ndi kupita ku manda a mdierekezi; satana wagonjetsedwa! Imfa yagonjetsedwa. Manda agonjetsedwa. Matenda agonjetsedwa. Zamatsenga zagonjetsedwa. Nkhwidzi zagonjetsedwa. Udani wagonjetsedwa. Kusayanjanitsika kwagonjetsedwa. Kukhuthala kwagonjetsedwa. Kumvazawekha kwagonjetsedwa. Chirichonse chagonjetsedwa. Khristu ndi Mgonjetsi wamkulu!

Apo, taonani Mgonjetsi wamphamvu, (anatero wandakatulo)
Apo, taonani Iye pa mbalambanda,
Pakuti Iye ndi Mgonjetsi wamphamvu,
Pamene Iye anang'amba chophimba pakati.

79 Iye anang'amba chophimba chimenecho chimene chinkamubisa munthu kwa Mulungu, ndipo tsopano Mulungu akukhala pakati pa anthu. Iye anang'amba chophimba chija chimene chinkawabisa machiritso a Mulungu. Iye anang'amba chophimba chija chimene chinkabisa madalitso a Mulungu. Iye anang'amba chophimba chija chimene chinkabisa chimwemwe cha Mulungu. Iye anang'amba chophimba chija chimene chinkabisa mtendere wa Mulungu. Tsopano chophimbacho chinang'ambidwa pakati. Ndi Magazi Ake Omwe, Iye anayenda ngati Mgonjetsi! Nkhondo yatha, Iye anatsimikizira izo kwa ife mu chiukitsiro Chake. Ndipo tsopano Mzimu Woyera ndi mboni, umene watumizidwa kuti udzatilondolere ife.

80 O Mulungu wa Muyaya, ngati pangakhale wina pano mmawa uno, amene wangowayawaya, kulowa ndi kutuluka, kuchokera ku msewu wawukulu, kumagwera mmphepete mwanjira; sanakhozepo kuyenda molondola pakati pomwe, ndi ngwazi zazikulu, ngwazi zazikulu zimene zimayenda pakati pa msewu wawukulu; ife tikupemphera, mmawa uno, kuti iwo akapereke zawo zonse kwa Inu, ndipo atulukire ndi kudzasangalala chigonjetso chachikulu ichi chimene chapambanidwa ndi Ambuye wathu amene wawuka. Perekani izi, Atate, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Khristu.

81 Ndipo pamene ife tidakali ndi mitu yathu chiweramire. Ndikudabwa, mu kamphindi aka kanthawi, kuti ngati inu mungakwezere manja anu kwa Khristu, ndikuti, "Khristu, ine ndikuyamikira, ine sindidzachita Nanu konse manyazi. Ine ndangokhala wa manyazi pang'ono." Mulungu akudalitseni

inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu, inu. Oh, mai, manja akungopita paliponse! "Ine ndakhala wamanyazi pang'ono. Ine ndakhala ngati wochita manyazi. Ndipo ine ndikuwawona malo anga kwenikweni tsopano. Ine sindinkayenera kuchita zimenezo konse. Ine ndimayenera kuima powonekera, ndikupereka umboni wanga! Ine ndizikhala ndendende chimenecho. Ine ndizimuuza aliyense, 'Ine ndabadwanso mwatsopano.' Ine ndizimuuza aliyense, 'Ine ndalandira Mzimu Woyera.' Ine sindikuchita manyazi ndi Uthenga, pakuti Iwo ndi Mphamvu ya Mulungu ku chipulumutso. Ine ndikufuna kukhala Mkhristu weniweni wopita chitsogolo. Ine sindinakhalepo. Koma, mwakuthandizidwa ndi Mulungu, kuyambira mmawa wa Isitara uno, ine ndikakhala. Ine ndikakhala." Winawakenso akweze manja anu tsopano ife tisanapemphere? Mulungu akudalitseni inu, inu, inu.

82 Mai, tayang'anani pa zigamulozo! Pafupifupi twente-faivi kapena sate, akhala pakati pa gulu laling'ono ili la anthu mmawa uno, apanga chigamulo. Kuyambira mmawa wa chigonjetso chachikulu ichi, iwo akatero, mwa chisomo cha Mulungu, akaima poyera ndipo sakachita nawo manyazi Uthenga, pakuti Iwo ndi Mphamvu ya Mulungu kwa chipulumutso.

83 O Mulungu, pamene manja awa akwera mmwamba, ndipo nyimbo ikumveka mokoma chotsika mu msewu, pamene ife tadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo, pakuti Inu munanena, "Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene ananditumа Ine, ali nawo Moyo Wosatha." Iwo adutsa kuchoka ku imfa kupita ku Moyo, chifukwa Inu munasanduka imfa kuti iwo adzakhale Moyo, kupyolera mu chiukitsiro Chanu. Inu munapangidwa wotsika kuposa Angelo, munabwera pansi pano kuti mudzakhale munthu, munatuluka mu Fiofane yaikulu iyo kuchokera Kuseri, imene inasandulika thupi ndipo inali ndi Magazi, ndipo munakhetsa Magazi amenewo, kuti Inu mudzakhoze kutipangira njira yothawirapo ya ife tonse. Ndiye simunangochita kokha izo, (ife timawerenga izo mu Baibulo), koma Inu munadzatsimikizira izo, mosalephera, powuka kuchokera kwa akufa, ndi kuwukitsa akufa pamene Inu munali kuno pa dziko lapansi; osati zokhazo, koma Inu munapereka, Inu mwazipanga izo kukhala zotsimikizika pawiri, monga Inu munachitira kwa Abrahamu; tsopano, pambali pa zimenezo, Inu munautumizanso Mzimu Woyera kuti udzakhale mboni. Ndipo ife tiri nako Kukhalapo Kwake kodala ndi ife, ndiponso mwa ife, kutilondolera ife, kutitsogolera ife mu Choonadi chonse ndi Kuwala.

84 Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha manja ambiri awa amene anakwezedwa mmwamba, mmawa uno, akuti, "Ine tsopano ndikumutenga Khristu ngati wanga." O Mulungu, ngati

iwo sanayambe abatizidwapo mmadzi, kuimirira imfa yaikulu, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro cha Ambuye wawo wodala, mulole iwo abwerere ku msonkhano mmawa uno, abweretse zovala zawo, ndipo okonzekera kukalowa mu dziwe lozizira ili. Perekani izi, Atate.

85 Tidalitseni ife. Mutikhululukire ife machimo athu. Ife tikupatsani Inu matamando, kudutsa mu mibadwo imene ikudza. Pamene nkhondo yonse idzatha, pamene utsi onse udzaumitsidwa, ndipo chimwemwe chonse chatha, za milomo ya dziko lino, kumene ife timakutamandani Inu ndi chirichonse chimene ife tiri nacho, ife tikuyenera kudzakhala ndi maliwu atsopano, zolengedwa zatsopano, kuti tizidzakulemekezani nazo Inu. Mulole tikalowe mkati mmenemo ndiye ndi chimwemwe. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Khristu. Ameni!

86 Tiyeni ife tiime ku mapazi athu tsopano . . . ? . . . Musaiwale misonkhano, hafu pasiti naini. Pitani kunyumba, mukadye kadzutsa wanu. Mubwererenso, ife tikuyembekeza kudzakhala ndi inu tsopano. Ndipo kenako usikuuno, kumbukirani. Ine ndikuyenera kuti ndichokepo masana uno, kukawerenga ndi kupemphera.

87 Pakuti ine ndikunena kwa inu, kuti, Khristu alimoyo, Iye si wakufa. Ndipo ine ndikukhulupirira, ndi mtima wanga wonse, Iye adzakhala mchipinda chomwe chino usikuuno, kuti adzawonetsere kuti Iye ali moyo, kuti adzachite zinthu zomwe zija zimene Iye anachita pa mmawa woyamba wa Isitara uja ndi kudutsa ulendo Wake wa moyo. Ngati izo siziri chomwecho, ndiye kuti ine ndakhala ndiri mneneri wabodza. Ndine wokondwa kwambiri kudziwa kuti mu ora lopambana la mdima ili limene ife tikukhalamo tsopano, pamene chiyembekezo chonse, mwakuwoneka, chapita; Khristu, Thanthwe lolimba ife tikhoza kuyimapo, maziko ena onse ndi mchenga wotitimira. Chabwino.

88 Nyimbo yathu yaying'ono, yobalalikira, ya *Tenga Dzina la Yesu ndi Iwe*. Aliyense, pamodzi tsopano.

Tenga Dzina la Yesu ndi iwe,
Mwana wa chisoni ndi watsoka;
Lidzakusangalatsa ndi . . .

89 Tembenukirani, ndipo mugwirane chanza, ndikuti, "Matamando kwa Ambuye," kwa winawake wa pambali panu. Chabwino, Ambuye adalitsike . . . ? . . .

Chiyembekezo cha dziko ndi chimwemwe cha
Kumwamba;
Dzina lofunika, Oh lokoma bwanji!
Chiyembekezo cha dziko ndi chimwemwe cha
Kumwamba.

90 Tsopano aliyense ayang'ane mbali iyi? Tiyeni ife tingomulemekeza Iye. Tiyeni tingokweza manja anu, ndikuti,

"Zikomo Inu, Ambuye, chifukwa chopulumutsa moyo wanga." Chabwino, aliyense!

Zikomo Inu, Ambuye, chifukwa chopulumutsa
solo yanga.
Zikomo Inu, Ambuye, chifukwa chondipanga
ine wamphumphu.
Zikomo Inu, Ambuye, chifukwa chopereka
kwa ine,
Chipulumutso Chanu chachikulu chodzadza
ndi chaulere.

91 Ndi chinthu chodala bwanji! Kodi inu mumamukonda Iye? Nenani, "Ameni." Oh, a . . . Chirichonse chamalizidwa tsopano, ana. Chirichonse chatha, kulibenso nkhondo, kulibenso zochitika za nkhondo, palibe kalikonse kamene inu muyenera kuchita; izo zinachitika kale. Ife tizingosangalala! Oh, mai! Ife ndi amphumphu, mwa Iye!

. . . potsamira,
Wotetezeka ndi wosamalidwa ku zowopsya
zonse;
Potsamira, potsamira,
Potsamira pa Nkono wosatha.

Oh, nzokoma bwanji kuyenda mu msewu wa
amwendamnjira,
Potsamira pa Nkono wosatha;
Oh, momwe mpita umawalira tsiku ndi tsiku,
Potsamira pa Nkono wosatha.

Potsamira, potsamira,
Wotetezeka ndi wosamalidwa ku zowopsya
zonse;
Potsamira, potsamira,
Potsamira pa Nkono wosatha.

Inu amene mungathe, ndipo muli ndi kampango, katulutseni iko.

. . . oh, potsamira,
Wotetezeka ndi wosamalidwa ku zowopsya
zonse;
Potsamira, potsamira,
Potsamira pa Nkono wosatha.

Tsopano Baibulo lanu!

Potsamira, potsamira,
Wotetezeka ndi wosamalidwa ku zowopsya
zonse;
Potsamira, potsamira,
Potsamira pa Nkono wosatha.

92 Icho ndi chiyani? Wosamalidwa ndi wotetezeka, konsekonse, zonse zamalizidwa, nkhondo yatha, chisindikizo chomaliza chamatulidwa, Iye wakwera mmwamba. Aleluya!

Potsamira, potsamira,
Wotetezeka ndi wosamalidwa ku zowopsya zonse;
Potsamira, potsamira,
Potsamira pa Nkono wosatha.

93 Tsopano tiyeni ife tiweramitse mitu yathu kuyang'ana ku fumbi kumene Mulungu anatitengako ife, kumene tsiku lina ife tidzakwera mmwamba kuchoka ku fumbi la mdziko lapansi. Pakuti, Ambuye wathu, anabweretsedwa kuchokera ku fumbi, anapita mu fumbi, kuti adzatipatse ife Mzimu Wake wachisavundi, Iye anakwera kuchokera ku fumbi, ndipo iwo onse amene ali mwa Iye, adzakwera limodzi ndi Iye tsiku lina, kupita ku madera a odalitsika.

94 Pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Ine ndikuwona M'bale Smith ali pakati pathu, mmawa uno, m'busa wa Church of God; anandiimbira ine usiku watha. M'bale Smith, kodi inu mungadzukepo. Ine ndikudabwa tsopano, kuti ngati M'bale Smith angadzatibalalitse ife ndi mawu a pemphero. Pamene inu mukuthamangira ndiye ku nyumba zanu, ndi kukakhala ndi kadzutsa wanu. Kukabwereranso ku msonkhano wa Sande Sukulu, ndi utumiki wa ubatizo, mwamsanga zidzayambika pa hafu pasiti naini. Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu, pamene M'bale Smith akutibalalitsa ndi pemphero.

Mgonjetsi Wamkulu Ndi Wamphamvu CHA57-0421s

(The Great And Mighty Conqueror)

Misonkhano Ya Chitsitsimutso Cha Isitara

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, unaperekedwa mu Chingerezi pa Isitara Lamlungu mmawa pa kutuluka kwa dzuwa, Epulo 21, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2020 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org